CHIYAMBI

ZINTHU ZITATU ZOYANG'ANIRA ZA MOYO WA DZIKO LAKUGWA

1. **Mayesero sapeweka.**

   Okondedwa musazizwe ndi mayesedwe amoto adakuwerani inu akhale chakukuyesani, ngati chinthu chachilendo chachiktika nanu. (1 Petro 4:12)

   "Zinthu izi ndalankhula ndi inu, kuti mwa Ine mukakhale nawo mtendere. M'dziko lapansi mudzakhala nacho chivuto, koma limbikani mtima; ndalilaka dziko lapansi Ine." (Yohane 16:33)

   Ndipo onse akufuna kukhala opembedza mmoyo mwa Khristu Yesu, adzamva mazunzo. Koma anthu oipa ndi onyenga, adzaipa chiipire, kusokeretsa ndi kusokeretsedwa. (2 Timoteo 3:12-13)

2. **Mayesero "amatiwumba" kapena "kutiphwasula."**

3. **Ozunzidwa amalephera kusuntha kudutsa pakufunsa "chifukwa" ndi kukhalabe okhazikika mu ululu wawo.**

MAWU OCHOKERA KWA MULUNGU KWA IWO AMENE DZIKO LAWO “LIKUGWA.”

Yakobo, kapolo wa Mulungu ndi wa Ambuye Yesu Khristu kwa mafuko khumi ndi awiri a m’chibalaliko; ndikulankhulani. 2 Muchiyese chimwemwe chokha abale anga amene mukugwa mmayesero a mitundu mitundu; 3 pozindikira kuti chiyesedwe cha chikhulupiriro chanu chichita chipiriro. 4 Koma chipiriro chikhale nayo ntchito yache yangwiro, kuti mukakhale angwiro ndi opanda chirema, osasowa kanthu konse. (Yakobo 1:1-4)

1. **Kodi chimene ndingawongolere ndi chiyani pamene dziko langa likugwa?**

   Yankho: <u>KHALIDWE LANGA</u> (Yakobo 1:2)

   “Muchiyese” – unikani, werengetserani, sankhani.

   “Chimwemwe chokha” – khalidwe = kutanthauza kwenikweni, “chosasakaniza, kapena chimwemwe choyera changwiro”

   “Mayesero” - ozungiliridwa ndi

2. **Kodi ndichite chiyani kuti ndikwaniritse lero?**

   Yankho: <u>PILIRANI / LIMBIKANI</u> (Yakobo 1:3)

   “Podziwa” – pochitachita = maonedwe

   “Kuyesa” – kutsimikizira, kuyeretsa, kusonyezera ngati chenicheni.

   “Kupilira” – kupo meno = mphamvu zokhazikika

3. **Ndili ndi chiyembekezo chotani cha mawa?**

   Yankho: Mulungu adzatenga <u>CHOIPITSITSA</u> ndi kuchigwiritsa ntchito ku <u>CHABWINO</u> kwambiri cha ine. (Yakobo 1:4)

   “Lolani chipiliro” – Lolani, mugwirizane ndi ntchito za Mulungu chotero kuti mudzakhale…

   “Changwiro” – chokhwima, chakucha, chokula msinkhu.

   “Chomalizika” - chodzadza, magawo onse okwanira bwinobwino ndi okula bwino, osasowa kanthu.

MMENE MULUNGU AMAGWIRITSIRA NTCHITO MAVUTO KUTIKHWIMITSA IFE

1. Timakakamizidwa KUDALIRA Mulungu pa mulingo wina. Kungotisiya tokha , timayamba kukhala odzidalira, onyada, ndi osakhudzika kwa Mulungu.
2. TIMASIYITSIDWA kuchoka pa zosakhazikika za changu ndi zinthu za dziko za moyo uno. Timakakamizidwa KUZIWUNIKANSO pa makhalidwe athu, zofunikira kwambiri, kudzipereka, ndi tsogolo.
3. Mayesero amatilola KUCHITIRA UMBONI woyambirira wa zoona ndi mphamvu za Mulungu. Zosowekera zathu zimakhala chonyamulira chisomo cha Mulungu; mavuto athu chinthu cha mphamvu Zake..
4. Amatumikira UMBONI wozizwitsa ku dziko losakhulupirira. Mmene timapilira zokhoma kumasonyeza ku dziko mmene Mulungu weniweni aliri.
5. Timakhala anthu okhudzika, osamala, ndi chifundo monga NGATI KHRISTU. Iwo amene anakhumudwitsidwa kwambiri amakondanso mozama

MAFUNSO OKAMBIRANA:

1. Gawanani chokumana nacho chowawa mmoyo wanu wammbuyo (ngakhale chili chovuta) chinakhala ndi zotsatira zabwino mmoyo mwanu.
2. Ngakhale zili zabwinobwino, ndi chifukwa chiyani kuli koyenera kufunsa mopitilira kuti, “chifukwa chiyani?”
3. Kodi tsopano ndi dera liti la mmoyo mwanu limene likukwanira kukhala yesero, kapena “chophwanya dziko”?
4. Tengani mphindi pang’ono ndi kuyenda mu mafunso a atatu a chiyani amene Mulungu akutipatsa mu Yakobo 1:2-4.
5. Kambiranani za mmene mungayikire choona ichi mu zochitachita za nyengo zanu zatsopano. Mutseke ndi nthawi yotukulirana wina ndi mnzake mu pemphero.